Malamulo oyenera kutsatidwa ndi anthu ogwira ntchito zopereka chithandizo

Ogwira ntchito zopereka chithandizo **adzalangidwa, ngakhale kuchotsedwa ntchito kumene, chifukwa cha mchitidwe wosavomerezeka wokhudzana ndi kugonana**. Nawa malamulo oyenera kutsatira:

- Ogwira ntchito **sali oledwa kupanga zibwenzi zogonana ndi munthu aliyense wosafika zaka 18, ngakhale zitakhala kuti zimenezi ndizovomerezeka m'dziko lawo.** Kunena kuti iye sanadziwe zaka za munthu yemwe wagonana nayeyo si chifukwa chomveka.

- Ogwira ntchito **sali ololedwa kupatsa anthu ena ndalama, ntchito, katundu ndi zithandizo zina ngati malipiro a kugonana.** Ndipo sakuloledwa kutenga katundu yemwe ndi thandizo loyenera kuperekedwa kwa anthu ovutika n'kulipirira zinthu zimenezi. Iwo sakuyenera kulonjeza zinthu izi kuti anthu ena avomere kuchita zinthu zomwe zingawachititse manyazi kapena kuwaphera ufulu. Zinthu zimenezi ndi monga kulipira ndalama kwa anthu oyendayenda kapena mahule ndi cholinga choti agonane nawo.

- Ogwira ntchito ali ndi mphamvu kapena kuti ulamuliro pa yemwe angalandire katundu ndi zithandizo zina. Izi zikutanthauza kuti ogwira ntchitowo ali ndi mphamvu zochuluka pa anthu ofuna chithandizo. Pa chifukwa chimenechi, mabungwe othandiza **amalimbikitsa kwambiri ogwira nthito awo kuti azipewa kupanga zibwenzi zogonana ndi munthu aliyense** yemwe akusowekera chithandizo chifukwa cha mavuto omwe amugwera. Zibwenzi zamtunduwu zimapangitsa anthu kuwona ngati ntchito zopereka chithandizo sizikugwiridwa mokhulupirika ndi modalirika.

- Ngati wogwira ntchito **ali ndi dandaulo kapena akukayikira,** kuti munthu wina wa m'bungwe lawo kapena wa m'bungwe lina akuphwanya malamulo pa nkhani ya kugonana, **akuyenera** kudziwitsa akuluakulu, potsatira **ndondomeko** zomwe zakhazikitsidwa m'bungwe lawo.

- Ogwira ntchito zopereka chithandizo **akuyenera kutengapo gawo pokhazikitsa** malo a ntchito abwino, osalekerera makhalidwe osayenera pa nkhani ya kugonana komanso afunika kulimbikitsa ogwira ntchito anzawo **kutsatira ndondomeko za makhalidwe oyenera pa ntchito. Atsogoleri onse** ali ndi udindo wothandizapo komanso kukhazikitsa dongosolo lothandiza kuti pa malo a ntchito papitirize kuchitika makhalidwe ovomerezeka.

Mfundo za IASC, zomwe zimanena za nkhaza zokhudzana ndi kugonana, zikupezeka apa: http://www.pseataskforce.org/uploads/tools/sixcoreprinciplesrelatingtosea_iasc_english.doc.
Uthengawu ukuchokera ku bungwe lowona za anthu okhudzidwa komanso za chitetezo ku nkhaza zokhudzana ndi kugonana la *IASC Task Team on Accountability to Affected Populations and Protection from Sexual Exploitation and Abuse*, ndi bungwe la anthu omasulira nkhani la *Translators without Borders,*